

EXAMINATION NO: _____



BLANTYRE SECONDARY SCHOOL CLUSTER

2026 MALAWI SCHOOL CERTIFICATE OF EDUCATION MOCK EXAMINATION

CHICHEWA

Subject Number: M032/III

Thursday, 26 February

Time Allowed: 2 hours

8:00 – 10:00 am

PAPER III

(Malikisi 70)

Instructions:

1. Onetsetsani kuti pepala ili lili ndi masamba osindikizidwa khumi.
2. Pepalali lili ndi magawo awiri: A ndi B. Yankhani mafunso onse m'magawo onsewa
3. Lembani **nambala yamayeso** pamwamba pa tsamba **lililonse la pepalali**
4. Muchitembulo chili pambalichi, onetsani funso lililonse lomwe mwayankha pochonga mubokosi lomwe lili kutsogolo kwake.
5. Perekani pepalali kwa oyang'anira mayeso nthawi ikakwana

Funso	Chongani funso ngati mwayankha	Muno musalembemo	
1			
2			
3			
4			
Total			



Gawo A (Malikisi 30)

Nkhani za Mchezo ndi zolembedwa

Langizo: Yankhani mafunso onse m'gawoli.

1. Werengani ndakatulo ili m'munsiyi ndipo muyankhe mafunso otsatirawo pa mizere ili pansi pa funso lililonse.

KALATA KWA AMAYI

Ndinu amayi mwandilera
Ndi chithandizo cha atate.
Munandisamala pondinyamula,
Chimwemwe chikula mwa inu.

Zinali choncho kaamba ka ine.
Ndinalidi kalirole wanu
Pogona mumandiyang'ana.
Kunena zoonu Mayi, munandikonda.

Pamene ndinkalira munandiyimbira
Nyimbo yokoma, yondigonetsa.
Lululu! Lululu! Inalidi.
Nyimbo yonditonthozera inu amayi.

Nkumbukira pamene munkandisisita
Pamsana, ine chimwemwe mumtima.
Inu munali woyamba kundipsopsonapsopsona
M'dziko lapansi pano amayi.

Mwazi wanu unali kudya kwanga.
Msana wanu unali chikwa changa.
Miyendo yanu inali chikochikale.
Ndipo mkokeri munali inu Mayi.



MAFUNSO

- a. i. Tchulani yemwe akuyankhula m'ndakatuloyi.
_____ (Malikisi 1)
- ii. Lembani kufunika **kumodzi** kwa ndakatuloyi.

_____ (Malikisi 2)
- b. Pezani chitsanzo **chimodzi** cha zipangizo izi kuchokera m'ndakatuloyi:
- i. kubwereza lembo lamtsekulanjira kumapeto
_____ (Malikisi 1)
- ii. umunthu
_____ (Malikisi 1)
- c. Tchulani kamvekedwe ka zoyankhula mu ndakatuloyi.

_____ (Malikisi 2)
- d. Perekani matanthauzo a mawu awa malingana ndi ndakatuloyi.
- i. chikwa
_____ (Malikisi 1)
- ii. chikochikale
_____ (Malikisi 1)
- e. Tchulani zipangizo izi malingana ndi ndakatuloyi.
- i. mwazi
_____ (Malikisi 1)
- ii. munkandisisita
_____ (Malikisi 1)
- f. Pezani kuchuluka kwa mapande mu mzere uwu: 'Nyimbo yokoma, yondigonetsa'.
_____ (Malikisi 1)
- g. Kodi ndakatuloyi ingalalutidwe tsiku lanji?
_____ (Malikisi 1)

- h. Fotokozani mfundo yaikulu **imodzi** kuchokera m'ndakatuloyi popereka umboni umodzi.

(Malikisi 2)

2. Werengani nkhani ili m'munsimu mosamala ndipo muyankhe mafunso otsatirawo.

DZIKO NDI LOZUNGULIRA

Khama anakaona London imene abale sanaione. Asanachoke, makolo ake adamulangiza kuti akasamale ndi akazi odziwa kudyera amuna.

Akutsanzikana ndi anzake, anamuza kuti akakhulupirike ndipo akakachita chibwana akagulitsa thanzi lake.

Tivine anali kuchita malonda usiku ndi usana. Anali kupita ku Zizulu, ku Dembeke kukagula matimati ndi kumakapikulitsa ku msika wa Plantaya kuti apeze ndalama zoti mwamuna wake apite ku Ulaya. Amakwera malole, mvula ndi mphepo ndi kumamusisita. Tivine anali nyenyezi. Amamukonda mwamuna wake Khama Khomba, wantali watindivu take tonga tonde.

Tivine anaonda panthawi imene amathamangathamanga kufuna ndalama zoti mwamuna wake ayendere. Anafika potsika sikelo ndi ma kilogalamu asanu ndi atatu.

Khama sanalabadire za lonjezano lake lija. Atangotha sabata imodzi anapeza ntchito yosamalira nkhalamba ina. Masiku oyamba anayetsa kumamuimbira lanya mkazi wake uja. Kumuuza za mmene London imaonekera. Adamulonjeza adzatumizira tikiti kuti nayenso adzakaone ku Ulaya adzakananale.

Khama sanasamale kuti ndalamazo amazipezanso movutikira kuiwala chimene anapitira kunjako. Thupi lake losiririka la thanzi linangokhala phwando la matenda osiyanasiyana ndipo lidasanduka bango.

Kuyankhulana ndi mkazi wake kunachepa. Kenako anasintha nambala ndi kusiya kuyankhulana naye. Kenako anapezana ndi mayi wa ku Limbabwe, apa ndiye



anayiwaliratu za kumudzi. Analonjezana za ukwati. Koma tsiku lina anangopeza kuti katundu yense wamera mapiko ndipo mkaziyo sanamuonenso.

Apa ndi pamene anakumbukira mkazi wake kumudzi. Akaganiza za mwana wake, Mwali kuti akalandira chiyani ankangopukusa mutu.

Ndi katundu ochepa amene anatsala naye anaganiza zokwera ndege imene imanyamuka nthawi imeneyo kubwerera kwa mkazi wake. Anavutikira kupeza nambala ya Tivine, koma amene anamupatsa nambalayo sananene chilichonse chokhudzana ndi moyo wa Tivine.

Khama anamutumizira uthenga wolemba pa lamy za tsiku ndi nthawi imene ati adzafikire pa bwalo la ndege la Lileka.

Nthawi yonseyo palibe tsiku limene anatumiza thandizo kwa Mwali. Anatengeka ndi zochitika za ku Ulaya. Maganizo anamuvuta Khama.

Zitseko za ndege zinatsegulidwa ndipo anthu anayamba kutsika kulondola khomo limene limafikira alendo. Thupi la Khama linayoyoka. Koma Tivine anatolera thupi moti kukongola kumene kumabisala mu umphawi uja kunatumphuka. Anali atavala mochititsa kaso moti Khama sanathe kumuzindikira.

Tivine anamuzindikira Khama ndipo anapita pamene anaima kumukumbatira namulandira ku Nalawi uku akumwetulira. Anatenga katundu wake kukalongedza mu galimoto yake la mtundu wa Prado.

Ali mkati moyenda mu mzinda wa Pulantaya, mafunso ambiri amazungulira m'mutu mwa Khama koma anali wamanyazi kuti afunsa bwanji. Tivine anzipeza kuti izi? Anadutsa mkati mwa tawuni kulunjika ku Damiwawa.

Kenako galimoto ija inaima kunja kwa chinyumba chosanjikizana. Pageti pali alonda anayi ndi agalu awiri, maluwa onunkhira bwino ali ponseponse.

Khama anatengedwa kulowa mnyumba. Tivine ndi abambo aja atalowa, m'chipinda muja kamwana kankathamanga kumawazungulira.

“Bambo, awa ndi Bambo Khomba amene anali amuna anga ndinkakuuzani aja.”

“A Khomba, ndili ndi chikhulupiriro kuti munakwaniritsa zimene mumafuna m'moyo wanu. Ndinayesetsa kupeza njira yoti ndipeze ndalama zoti inu mupitire ku Ulaya kuti mwina moyo wathu usinthe. Zinali zochititsa manyazi kwa ine ndi mwana wanga Mwali. Tendayi, mkazi amene munayesa kuti akhale mkazi wanu anandiuza zonse. Chimene

simunadziwe ndi chakuti Tendayi anali m'bale wanga amene anali wachitatu kubadwa. Iye anatsalira ku Limbabwe pamene makolo anabwerera kuno ku Nalawi. Atasesa katundu wanu anabwerera ku Limbabwe kwa mwamuna wake. Tendayi anamwalira miyezi iwiri yapitayo ndi matenda a Edzi. Bambo Khomba, simungapikisane ndi dziko. Dziko ndi lozungulira ili.”

Tivine anayang'ana kukhoma kenako anamuyang'ana Khama.

“Awa ndi amuna anga tsopano” anatero akuloza abambo ena aja. “Ndipo mwana akusewera apoyo ndi mwana wathu, mlongo wake wa Mwali.”

Nthawi yomweyo Khama adagwa pansi nakomoka.

Mafunso

- a. Tchulani chinthu chimodzi chachitika pa pachikwera pankhaniyi.

_____ (Malikisi 2)

- b. Perekani chitsanzo chimodzi cha chisokonezo cha pakati pa munthu ndi munthu kuchokera m'nkhaniyi.

_____ (Malikisi 1)

- c. Ndi chinthu chiti chomwe yemwe adathandiza Khama ndi nambala Tivine sadafune kuuza Khama?

_____ (Malikisi 2)

- d. Pezani ampangankhani awa kuchokera m'nkhaniyi:

- i. mpangankhani wamkulu

_____ (Malikisi 1)

- ii. mpangankhani wopaza

_____ (Malikisi 1)

- iii. mpangankhani wosintha

_____ (Malikisi 1)



- e. Fotokozani njira imodzi yonetsera khalidwe la Tivine m'nkhaniyi.

_____ (Malikisi 2)

- f. Pezani zipangizo izi kuchokera m'nkhaniyi:

i. kalosera

_____ (Malikisi 1)

ii. chiyerekezero

_____ (Malikisi 1)

iii. voko

_____ (Malikisi 1)

- g. Fotokozani mfundo yaikulu **imodzi** kuchokera m'nkhaniyi.

(Malikisi 2)

Gawo B (Malikisi 40)

Langizo: Yankhani mafunso awiri okha m'gawoli m'ndime zofotokozedwa bwino.

NTHONDO (S J Nthala)

3. a. Tsimikizani popereka mfundo **zinayi** zosonyeza kuti nzika za m'mudzi wa a Chembe zidali zomvana pa chikhalidwe ndi miyambo.

(Malikisi 20)

KAPENA

- b. Fotokozani mfundo zinayi zosonyeza kuti Nthondo adali watsoka asanatembenuke mtima malingana ndi buku la Nthondo.

(Malikisi 20)



KHOSWE WA PADENGA

4. a. Tsimikizani popereka mfundo zinayi kuti kusakhulupirika ndi mfundo imodzi mwa mfundo zazikulu m'chisudzochi.

(Malikisi 20)

KAPENA**MUDZI WA MFUMU TANDWE**

- b. Fotokozani popereka mfundo zinayi kuti mudzi wa Tandwe ndi wamakhalidwe oipa.

(Malikisi 20)
